

Momwe tingawiritse ntchito mitengo jobwezeretsa chonde m'nthaka

Girisidia:

Yambani kuthena pamene usinkhu wa mitengo waposera mita imodzi. Pa usinkhu umenewu mitengo izakhala ndi mizu yambiri ndi yokhwima bwino.



Thenani ndi kuyala nthambi mmipata.



Musanayambe kulima: ikani masamba ndi zinyalala mumpata ndipo limani mizera.

Ngati mwalima kale mizera: gawani mizera pakati, ikani masamba ndi kukwirira ndi dothi.


Chitani izi nsangansanga mukangotsiriza kuthena kuti mchere wa mbeu usachoke ndi dzuwa, mvula ndi mphepo.

Mitengo yotsalayo itengedwe ndi kukapangidwa nkhu.



Kubwezeretsa chonde mnthaka pobzala mitengo m'munda

CHICHEWA



*Laurence Mathieu-Colas
Goulven Le Bahers*

November 2009

Translation : Mr. Laston M. Makina

This document has been produced with the financial assistance of the European Union. The contents of this document are the sole responsibility of Inter Aide and can under no circumstances be regarded as reflecting the position of the European Union.

Za chonde m'nthaka

Zomera zimafuna dzuwa, madzi, nthaka ndi zakudya za mbeu zimene zimapezeka m'nthaka (NPK, zowolerana...).

Zakudya za mbeu ndi zowolerana zimasungika m'nthaka. Kusowa kwa zinthu zimenezi, kuma pangitsa kuti nthaka ikhale yopanda chonde.

Kunena zowona, mchere wa m'nthaka ungapezeke pogwiritsa ntchito feteleza. Koma feteleza ndi wodura ndipo sabweretsa chonde.

Zowolerana ndi zimene zimasunga chinyontho m'nthaka. Zimasunganso zakudya za mbeu m'nthaka ngati zimene zimapezeka mufeteleza.

Kusoweka kwa zowolerana m'nthaka ndilo vuto lalikulu m'Malawi muno.

Ngati zowolerana zitabwezeretsedwa m'nthaka, ndiye kuti zokolola zikhala zochuluka m'njira yokhazikika ndipo feteleza sazafunika kwenikweni ndipo azagwira ntchito moyenera.

Tingabwezere bwanji chonde m'nthaka yathu?



Mitengo ya mgulu la nyemba itha kubzalidwa m'munda pofuna kuthetsa vutoli. Mitengoyi imabweretsa kuwolerana ndi mchere umene umafunika kuti mbeu zikule bwino.

Zochokera mu:

(1) "Agroforestry practices in Malawi", Malawi Agroforestry Extension Project - Government of Malawi, USAID, Washington State University

(2) "Tephrosia in pest control", ICRAF Southern Africa

Momwe tingagwiritse ntchito mitengo jobwezeretsa chonde m'nthaka

Msangu:

Kuonjedzera chonde m'nthaka:

Kugwa kwa masamba kumayambiro a nyengo ya mvula kumabweretsa chonde m'nthaka mwa chilengedwe kumathandizira kupanga malo oyenera kukhalamo tizirombo topezeka m'nthaka.

Ntchito zina:

Mtengowu umabereka zibalobalo zochuluka zomwe ndi zakudya zabwino za ziweto m'nyengo ya chilimwe. Umapereka nkhuni ndi matabwa abwino.

Popeza ndi umodzi mwa mitengo yochepa yomwe imakhala ndi masamba m'nyengo ya chirimwe, umakhala ndi m'thunzi wabwino kwa anthu ndi ziweto.

Ombwe / Mthuthu:

Kuonjedzera chonde m'nthaka:

Dulani mitengo pansu musanayambe kulima. Zikaomberedwa dzuwa kwa masiku awiri kapena atatu, yoyolani masamba mitengoyo gwiritsani ntchito zina kapena mupange nkhuni. Mutha kutsiya masambawo, kukwirira m'mizera kapena kuojeka. Tsatirani izi m'nyengo zonse za ulimi.


Kugwiritsa ntchito ngati mankhwala:

Pululani masamba ndi kutsinja mu ntundo. Nyikani masamba kwa maora awiri kapena wiritsani kwa mphindi makumi atatu (kuti agwire ntchito bwino, masamba ochuluka 1Kg anyikidwe m'madzi okwanira malita asanu).


Sefani ndi nsaru ndipo poperani ndi mpope. Pofuna kuti mankhwala agwire kumasamba thirani sopo pang'ono m'mankhwala. Ndi bwino kuti mankhwala azigwera pa zilombo. Mankhwala amagwira ntchito masiku asanu ndi awiri ndiye muyenera kuthiranso pakapita masiku amenewa.

Zitsanzo za kabzalidwe


Kubzala Girisia:




Kubzala Ombwe / Mthuthu:



Kodi mitengoyi imagwira bwanji ntchito?



Mitengo ya gulu la nyembayi imakhazikitsa chakudya cha mbeu chochokera mu mpweya (zikomo ku tizilombo tosaoneka ndi maso tomwe timakhala pa mizu). Tizilombo timeneti timapanga nchere wa mu mpweya kukhala nchere wa m'mera. Apa ndiye kuti chakudya cha mbeu chapezeka.




Mitengo yomwe mizu yake imalowa pansi kwambiri imathandizanso kutenga chakudya cha mbeu m'nthaka ya pansi kupita nacho m'nthaka ya pamwamba. Chakudya chichimachoka ku mizu kupita ka masamba. Masambawa akagwa m'nthaka, ndiye kuti chakudya cha mbeu chapezeka.

Mitundu ya mitengo iti yomwe tingagwitse ntchito?



Msangu: mtengo waukulu umene ungapange mchere wa mbeu ndi kuubwezera m'nthaka m'nyengo ya mvula zikomo chifukwa cha masamba obweretsa chonde. Mizu yache imalowa mozama ndipo imatenga zakudya za mbeu kuchokera m'nthaka ya pansi. Umapereka chonde m'nthaka kwa nthawi yaitali.

Girisidia: kamtengo kameneka kamabweretsa mchere wofunika ku mbeu m'nthaka. Ndipo umapanga m'thunzi wabwino, kupangira manyowa komanso nkhu. Umapereka chonde m'nthaka kuyambira chaka choyamba.



Ombwe kapena **Mthuthu:** kamtengo kakang'ono komwe kangabweretse chonde m'nthaka zikomo chifukwa cha masamba ache. Utha kugwiritsidwa ntchito ngati mankhwala oteteza mbeu ku mbozi. Umabwezera chonde m'nthaka kuyambira chaka choyamba.

Mitengoyi tingayibzale bwanji?

Mitengo yobweretsa chonde m'nthakayi, itha kufetsedwa ku nazale kapena kukangobzala mmunda. Njira yotsirizayi ili ndi ubwino wache imatenga nthawi yochepa chifukwa sipakhala ntchito ya kunazale. Komabe, imafuna kusamala kwambiri m'munda, makamaka nthawi ya chipalapala ndi bandila.

Kubzala m'munda: mitengo yatchulidwa m'mwambayi imabzalidwa m'njira izi:

Mtundu wamitengo	Kukonzetsera njere	Kuchuluka kwa njere pa phando	Kutalikirana kwa mapando
Msangu	Kukuta	ziwiri	10m x 5m pa nzera
Girisidia	Kunyika m'madzi kwa maora 24	ziwiri	Nzera umodzi pa mizera itatu iri yonse ya mbeu yeniyeni. Kutalikana kwa mapando 90cm m'mbali mwa nzera.
Ombwe / Mthuthu	Palibe	zitatatu	Nzera umodzi pa mizera iwiri iri yonse 30cm iri yonse, pakati pa mapando a mbeu yeniyeni.

Kuzama kwa mapando: Kuzama kwa mapando kukhale 1.5 mpaka 2 cm. Njere zikabzalidwa mozama kwambiri, sizingamere.

Kupatulira Msangu (mitengo zana limodzi yokulakula pa hekita):

Kukula kwa mtunzi	Kutalikana	Chiwerengero
Mamita 5	10m x 20m	Mitengo 50 pa hekita
Mamita 8	20m x 20m	Mitengo 25 pa hekita
Kupyola mamita 20	Chimodzimidzi m'mwambamu chotsani yosaoneka bwino ndi nthambi	Mitengo 15 mpaka 20 pa hekita